

# Tools and Training for Livelihood in Malawi - 2020/21

Kutukula Miyoyo ya Anthu ku Malawi popereka Zida  
ndi Maphunziro a Ntchito za Manja 2020/21

BOOK 8



Doris John

A project run by The  
Global Concerns Trust  
and funded by  
The Scottish Government

Ntchito imene bungwe  
la Global Concerns Trust  
likugwira ndi thandizo la  
ndalama lochokera ku  
boma la Scotland





The Global Concerns Trust is a Scottish based charity that aims to reduce poverty and empower vulnerable people through partnering organisations that implement sustainable grassroots development projects. We currently support projects in India, Kenya and Malawi.

We have worked with our partners in Malawi for 13 years to provide vocational training and start up tools to hundreds of adults with disabilities, helping them to start up small businesses and generate an income to support themselves and their families.

This booklet details The Global Concerns Trust's current project, Tools and Training for Livelihood in Malawi, funded by The Scottish Government. We have produced a film about this project, which can be viewed on our website [www.globalconcernstrust.com](http://www.globalconcernstrust.com)

**Registered Charity:** SC025640

Global Concerns Trust ndi bungwe la chifundo la mdziko la Scotland. Cholinga chake ndi kuchepetsa umphawi ndi kutukula anthu osowa pogwirizana ndi mabungwe amene amagwira ntchito zokhalitsa za chitukuko ndi anthu a Kumudzi. Pakali pano tikuthandiza ntchito za chitukuko ku mayiko a India, Kenya ndi Malawi.

Tagwira ntchito mogwirizana ndi mabungwe amene timathandizana nawo mdziko la Malawi kwa zaka 13 kupereka maphunziro a luso la ntchito za manja ndi zida zopangira bizinezi kwa anthu akuluakulu zikwi zikwi olumala, kuwathandiza kuti ayambe mabizinezi ang'ono ang'ono kuti azitha kupeza ndalama zowathandiza iwo eni pamodzi ndi maanja awo.

Buku ili likufotokoza tsatanetsatane wa ntchito imene bungwe la Global Concerns Trust likugwira ku Malawi yopereka zida ndi luso la ntchito za manja pofuna kutukula miyoyo ya anthu ndi thandizo la ndalama lochokera ku boma la dziko la Scotland. Takonza kanema ofotokoza za ntchito imeneyi, ndipo mungayipeze pa tsamba lathu la intaneti limene likupezeka pa [www.globalconcernstrust.com](http://www.globalconcernstrust.com)

# THE PROJECT

52% of households in Malawi do not have enough to eat. Poverty in rural areas is especially high. People with disabilities are more likely to live in poverty due to multiple barriers to accessing education, health care and employment. In addition, people with disabilities experience further challenges such as lack of disability aids and medical treatment, stigma and prejudice, higher chances of being subjected to violence, isolation and disempowerment. People with disabilities have been widely excluded from many development processes. Women and girls with disabilities live with double discrimination due to existing gender inequalities.

**This project aims to reduce poverty in Malawi by empowering adults with disabilities, equipping them with the skills and tools needed to be self sufficient and earn a living.**

We offer training to people with all types of disabilities including epilepsy, sight and hearing impairments and learning disabilities and mental health conditions. Tools and sewing machines are donated in Scotland and Northern Ireland and are refurbished by volunteers at the Scottish Tools for Self Reliance workshops in Edinburgh, Milltown and Aberdeen, The Ecology

Centre and the Tools for Solidarity workshops in Northern Ireland.

They are then shipped to Malawi and are used by our partners **MACOHA** and **KODO**, to provide vocational training in carpentry, tailoring and cane furniture making in Nkhotakota, Salima and Ntcheu districts.

Our trainees receive 6 – 12 months vocational training, business training, AIDS prevention, reproductive health and gender awareness training. When they have completed training, they receive the tools and machines they need to start their business.

All trainees also learn how to make organic manure, a skill they will pass on to their communities once they get home. This will help the fertility of the soil, reduce soil erosion, and increase agricultural yields, as well as saving people the cost of having to buy chemical fertilizer.

As well as the vocational training and tools, all graduates are also given solar powered home energy systems. Graduates will be able to use this technology to provide light for their families, increase their business output, and generate further income by providing mobile phone charging services.

Trainees receive on-going support and are visited by project workers at home to help them with the early stages of setting up businesses.



**Mavis Kankinga**



**Feston Benson**



**Alinape Sapulani**



**Alisenio Swinda**



# NTCHITO YAKE

Maanja 52 mwa 100 aliwonse (52%) ku Malawi alibe chakudya chokwanira. Mmadera a Kumudzi muli umphawi ochuluka. Anthu olumala ambiri akukhala mu umphawi chifukwa cha zinthu zochuluka zimene zimawalepheretsa kuti aphunzire, apeze chithandizo cha kuchipatala komanso ntchito. Kuonjezekerera pamenepo anthu olumala amakumananso ndi mavuto ena monga kusowa kwa zipangizo zoyendera, thandizo la mankhwala, kunyozedwa ndi kuyang'aniridwa pansu, kuchitiridwa nkhanza, kusolidwa ndi kuponderezedwa. Anthu olumala asiyidwa pa ntchito zochuluka za chitukuko. Amayi ndi asungwana olumala amasalidwa koposa chifukwa anthu saonedwa ngati ofanana. **Cholinga cha ntchitoyi ndi kuchepetsa umphawi ku Malawi potukula akuluakulu olumala, powapatsa luso ndi zida zofunika kuti akhale moyo odzidalira ndi kutha kupeza zosowa zawo.**

Timapereka maphunziro a ntchito za manja kwa anthu a ulumali osiyanasiyana monga, matenda a kugwa, osapenya, osamva, ovutika pophunzira ndi a ulumali wa mu bongo. Zida ndi makina osokera zimaperekedwa kwaulere ndi anthu ku Scotland ndi ku Mpoto kwa dziko la Ireland ndipo zimakonzedwanso ndi anthu odzipereka ku malo a bungwe la ku Scotland lokonza zida zothandiza anthu kukhala odzidalira (Scottish Tools for Self Reliance) ku Edinburgh, Milltown ndi Aberdeen, kumalo a zachilengedwe (The

Ecology Centre) ndi ku malo opanga zida zolimbikitsa umodzi (Tools for Solidarity workshops) ku Mpoto kwa dziko la Ireland. Zida ndi makinawa zimatuzidwa ku Malawi ndipo zimagwiritsidwa ntchito ndi mabungwe othandizana nawo a **MACOHA** ndi **KODO** kuphunzitsira ntchito za manja za ukalipentala, utelala ndi kukonza mipando ya nsungwi ku Nkhotakota, Salima ndi ku Ntcheu. Ophunzira athu amaphunzitsidwa kwa miyezi 6 mpaka 12. Amaphunzitsidwa ntchito za manja, kayendetsedwe ka bizinezi, kapewedwe ka HIV ndi AIDS, uchembere wabwino ndi kusasalana pakati pa abambo ndi amayi. Akamaliza maphunziro awo ophunzira amalandira zida ndi makina zowathandiza kuyamba ma bizinezi awo.

Ophunzira onse amaphunziranso kapangidwe ka manyowa kuchokera ku zinthu za chilengedwe (organic manure). Ili ndi luso limene ophunzira amakaphunzitsa anthu a kudera kwao akabwelera kumudzi. Manyowa akathandiza kuonjezera chonde mthaka, kuchepetsa kukokoloka kwa nthaka, ndi kuchulukitsa zokolola komanso kupulumutsa ndalama zogulira feteleza. Kuonjezera pa zida ndi luso la ntchito za manja ophunzira amalandiranso zipangizo za magetsi a dzuwa. Ophunzira amakagwiritsa magetsi adzuwa kuunikila mnyumba zao, kuti agwire ntchito ndi usiku omwe komanso kupha makwacha akamatchaja mafoni a anthu ena. Ophunzira amathandizidwa komanso amayenderedwa kunyumba ndi alangizi a ntchitoyi pofuna kuthandiza ophunzira pamene ayamba ma bizinezi awo.



Eliza Williams



Nasoni Mthambala



Ida Gofu



Oswald Banda



# KODO

**Our other partner in Malawi is KODO - a grass roots organisation based in Salima, that was founded by George Chimpiko, who himself has physical disabilities and who, since his retirement 13 years ago, has dedicated himself to helping other people with disabilities in Malawi.**

KODO provide training in tailoring and cane furniture-making to adults with disabilities in Salima district. They have trained over 250 adults with disabilities through this program (55% of which are women) and supported them to start up businesses.

It is George's determination and hard work that has seen the transformation of KODO from a one-roomed training space in his house, to a thriving educational community with a hall, hostel and training spaces, contained within 4 acres of sustainably farmed land, which produces enough food for the community.

Trainees live together at KODO for the duration of their training and for many of them, this will be the first time that they will have had the opportunity to leave their homes and meet other people with disabilities. The importance of these friendships, together with an increased sense of confidence and self-worth that comes from the training, cannot be underestimated.





Cane furniture training



Skill sharing workshop



George Chimpiko and Emma Duncan

# KODO

**Bungwe lina limene timagwira nalo ntchito limodzi ndi bungwe la KODO - ili ndi bungwe la ku Salima, linayambitsidwa ndi George Chimpiko, amene ndi munthu wa ulumali yemwe wadziperaka ku ntchito yothandiza anthu ena a ulumali ku Malawi kuyambira pamene anapuma ntchito dzaka 13 dzapitadzo.**

KODO imapereka maphunziro a utelala ndi kukonza mipando ya nsungwi kwa akuluakulu a ulumali mboma la Salima. Kudzera mu ntchito imeneyi aphunzitsa akuluakulu a ulumali oposerera 250 (Mwa iwowa 55 pa 100 aliwonse ndi amayi) ndipo awathandiza kuyamba ma bizinesi.

Chifukwa cha kulimbika kwa George KODO yakula kuchoka pa nyumba ya chipinda chimodzi chophunzitsira mnyumba mwao kufika pa malo ophunzitsira okhala ndi malo ochitira misonkhano, malo ogona ndi malo ophunzitsira zimene zili pamalo okula maekala 4 pamenenso pamatuluka chakudya chokwanira kudyetsa anthu onse a pa KODO.

Ophunzira pa KODO amakhala limodzi nthawi yonse ya maphunziro awo ndipo kwa ambiri mwa iwo imakhala nthawi yopamba kupeza mwayi ochoka kwawo ndi kukakumana ndi anthu ena a ulumali. Kufunika kwa mikumano yotere pamodzi ndi kukula kwa kudzikhulupilira kumene kumadza chifukwa cha maphunziro amene amalandira sikochepea.

# MACOHA

**Our two partners in Malawi are MACOHA (The Malawi Council for the Handicapped) and KODO (Kuthandiza Osayenda Disability Outreach).**

MACOHA (Malawi Council for the Handicapped) is a national organisation established by the Government of Malawi, to implement policies and strategies on disability. MACOHA are at the forefront of work to help men and women with disabilities to be more independent, self-sufficient, and recognised as equals within Malawian society. Their work includes supporting mainstream teachers to effectively include children with disabilities, providing access to cataract operations, orthopaedic clinics, ear health services, HIV/AIDS awareness training and supporting and offering training to mothers of children with disabilities.

MACOHA recognise that livelihood training is an essential part of supporting adults with disabilities in Malawi to be self sufficient. They have 2 vocational training centres in Lilongwe and Chiradzulu, but did not previously have the capacity to provide vocational training to adults living in the rural areas.

We started our partnership with MACOHA in 2007, introducing vocational training program for adults with disabilities in Dowa, Nkhotakota and Ntcheu districts.

Trainees are attached in groups of 4 or 5 to a local carpenter, tailor or cane furniture maker, and train with them as apprentices for 6 – 12 months. With this type of training they are able to learn how to run all aspects of an active business, as well as the necessary technical skills.



**MACOHA graduates**



# MACOHA

**Mabungwe awiri amene timagwira nawo ntchito ku Malawi ndi a MACOHA (Bungwe la boma lothandiza anthu olumala) ndi KODO (Kuthandiza Osayenda Disability Outreach).**

MACOHA ndi bungwe lokhazikitsidwa ndi boma la Malawi kuti lidzigwira ntchito zokhudza ulumali. MACOHA ikutsogolera ntchito yothandiza kuti abambo ndi amayi olumala akhale odziyimila paokha, odzidalira, ndi ofanana ndi anthu ena onse mdziko la Malawi. Zina mwa ntchito za MACOHA ndi kuthandiza kuti aphunzitsi athe kuphunzitsa ana onse alumali, kuthandiza kuti anthu ovutika maso, miyendo, kamvedwe athe kulandira thandizo lakuchipatala. Komanso kuzindikilitsa anthu za HIV & AIDS ndi kuphunzitsa komanso kuthandiza amayi a ana a ulumali. MACOHA imazindikila kuti

kuphunzitsa luso la ntchito za manja ndi gawo lofunika pa ntchito yothandiza akuluakulu omwe ali ndi ulumali kuti akhale odzidalira. MACOHA ili ndi malo awiri ophunzitsa luso la ntchito za manja ku Lilongwe ndi ku Chiradzulu. Kale MACOHA inalibe kuthekera kophunzitsa luso la ntchito ya manja akuluakulu okhala mmadela a mmidzi.

Mgwirizano wathu ndi MACOHA unayamba mchaka cha 2007, kuyambitsa maphunziro a luso la manja kwa akuluakulu mmaboma a Dowa, Nkhotakota ndi Ntcheu.

Ophunzira amayikidwa mmagulu a anthu 4 kapena 5 ndipo amaperekedwa kwa kalipentala, telala kapena okonza mipando ya nsungwi amene amawaphunzitsa kwa miyezi 6 kapena 12. Ndi maphunziro amenewa ophunzira amakhala ndi kuthekera koyendetsa bizinesi, komanso luso la ntchito za manja.



## Skill sharing workshops and post training support

Trainees receive on-going support and are visited by project workers at home to help them with the early stages of setting up their businesses. Through this continued contact with trainees, we are able to measure the long-term impact of training upon their lives, as well as continuing to assist them in any ways we can.

Graduates come back together to attend skill sharing workshops, where they share their experiences and challenges and give each other support and advice. The workshops are designed to support graduates to continue to work on product and skill development and graduate trainees use these workshops to share their individual progress and help each other to continue to develop their products and business strategies. This continued contact with fellow trainees and project workers helps graduates motivate, inspire and support each other.



**Skill Sharing Machoa**

## Misonkhano yogawana luso ndi upangili umene umaperedwa akamaliza maphunziro

Ophunzira amalandirabe upangili ndi kuyenderedwa ndi alangizi ku nyumba kwao kuti awathandize pamene akukhazikitsa ma bizinezi awo. Kudzera mu kuyendera ophunzira kotereku timatha kudziwa mmene maphunziro awo asinthira miyoyo yawo komanso kupitiriza kuwathandiza mmene tingathere.

Ophunzira otsiriza maphunziro amakumananso pa misonkhano yogawana luso, kumene amagawana za mmene mabizinezi ayendera komanso zovuta pa mabizinezi awo ndi kupatsana chilimbikitso ndi upangili. Misonkhanoyi imakonzedwa kuti ithandize ophunzira kupititsa patsogolo kakonzedwe ka katundu ndi luso ndipo pa misonkhanoyi ophunzira amagawana za mayendedwe a bizinezi zawo ndiponso amathandizana kuti apitilize kupititsa patsogolo kakonzedwe ka katundu ndinso kayendetsedwe ka bizinezi. Kukumana kawirikawiri kotereku pakati pa ophunzira ndi alangizi kumathandiza ophunzira kulimbikitsana ndi kuthandizana.



**Skill Sharing Kodo**



## Adapting to living with Covid-19

No one would describe 2020/21 as a good year! For the first time in the projects' 13-year history we were forced to stop our training. MACOHA and KODO quickly became involved in the prevention of Covid-19 through the provision of WASH facilities, information and masks to people with disabilities. Some of our graduates had to wait months before receiving their start-up equipment for their new businesses, due to our shipment being stuck in South Africa during lockdown. We were able to support them with a small financial fund which allowed them to rent equipment or start supplementary businesses whilst they waited. Our good news is that as a project we have been able to pull together, adapt and continue. Training resumed in Malawi in October 2020, 6 months after we stopped, our graduates in Malawi received their tools and the tool workshops in the UK have managed to continue to work towards our next shipment, despite the many challenges to their normal working practices in the UK. We have changed the way we conduct our training and skill sharing workshops to minimize chances of infection for trainees and staff. The patience, hard work and determination to keep things going demonstrated by everyone involved in the project has been immense.



## Kusintha pokhala mnyengo ya Covid-19

Palibe Munthu amene anganene kuti chaka cha 2020 mpaka 2021 chinali chaka chabwino! Kwa nthawi yopamba mu zaka 13 za mbiri ya ntchito imeneyi tinaumirizidwa kuyimitsa maphunziro amene timapereka. Mwachangu MACOHA ndi KODO anayamba ntchito yoteteza kufala kwa matenda a Covid - 19 popereka zipangizo zosambira mmanja, uthenga wa matendawa komanso zovala kukamwa kwa anthu a ulumali. Ophunzira athu ena anadikira miyezi ingapo asanalandire zida zogwiritsa ntchito pa ma bizinezi awo a tsopano chifukwa zidazo zinayimitsidwa ku South Africa pa nthawi imene boma linaletsa anthu kugwira ntchito (lockdown). Mnyengo imeneyo ophunzirawa tinawapatsa ndalama pan'gono zimene zinawathandiza kubwereka zida zogwilira ntchito kapena kuyambitsa mabizinezi ena pamene anali kudikilira zida zao. Uthenga wathu wabwino ngwakuti takwanitsa kupitiriza ntchito yathu. Ku Malawi maphunziro anayambikanso mwezi wa Okotobala mchaka cha 2020, miyezi 6 kuchokera pamene ntchitoyi inayimitsidwa. Ophunzira athu ku Malawi analandira zida zao, komanso malo okozanso zida ku Mangalande (UK) akwanitsa kupitiriza kukonza zida zoti tidzatumize mtsogolomo ngakhale pali zovuta zochuluka pa kagwiridwe kawo ka ntchito ku Mangalande. Tasintha mmene timapangira maphunziro ndi misonkhano ya ophunzira yogawana luso pofuna kuteteza ophunzira ndi ogwira ntchito kuti asatenge matenda. Kudekha, kulimbika ndi kudzipereka kumene anthu onse okhudzidwa anaonetsa kuti ntchitoyi idzipitilirabe ndi kwakukulu.





## BLESS JEKETE

**Bless Jekete** is 37 and lives with her mother in Ntcheu, Malawi. Bless has a hearing impairment. In 2019 she took part in the tailoring training run by MACOHA in Ntcheu. Before attending the tailoring training, Bless depended on piece-work such as farm work. On average she used to earn Mk 1000.00 per month. This was not enough to support herself and her mother and they often had no food. After graduating, Bless started a tailoring business, which she operates from home. Within a short time she was able to win the trust of many people from her village and Bless is now a successful tailor. She now earns an average of Mk 10,000.00 per month, increasing her monthly income by 900%. Bless is now the bread winner for her household and is able to provide for her mother and herself. Going without food is a thing of the past. From her income Bless has managed to build a two-roomed burnt brick house with iron sheets.

**Bless Jekete** ali ndi dzaka dzakubadwa 37 ndipo amakhala limodzi ndi Mayi ake mboma la Ntcheu ku Malawi. Bless ali ndi ulumali wa kusamva. Mchaka cha 2019 iye anachita nawo maphunziro a utelala amene bungwe la MACOHA limapereka ku Ntcheu. Mbuyomo Bless ankadalira kugwira maganyu mminda ya anthu ena. Nthawi zambiri iye ankapeza ndalama zokwanira Mk 1000.00 pa mwezi umodzi. Ndalama zimenezi sizinali zokwanira kudzisamalira iye mwini pamodzi ndi mayi ake, moti kawirikawiri ankakhala opanda chakudya. Atatsiriza maphunziro ake Bless anayamba bizinesi ya utelala ku nyumba kwao. Patangopita nthawi pan'gono anthu ochuluka a mmudzi mwawo anakonda luso lake ndipo pakali pano Bless ndi telala opambana, amapeza ndalama zokwanira Mk 10,000.00 pa mwezi, kuchulukitsa ndalama zopezeka pa mwezi ndi zikwi makumi asanu ndi anayi (900%). Tsopano Bless ndiye wafungatira banja lawo lonse ndipo akukwanitsa kusamala mayi ake pamodzi ndi iye mwini. Kugona ndi njala ndi mbiri ya kale. Ndalama zimene akupeza zamuthandiza Bless kumanga nyumba ya njerwa zowotcha ya zipinda ziwiri yofolera ndi malata.





**Harry Ernest** is 35 years old and comes from Nkhotakota district, Malawi. He has a leg disability. Harry's father died when Harry was young and Harry was raised by his mother, who depends on small holder farming. She could not afford school fees and Harry was forced to drop out while in form two. With no qualifications Harry could not find formal employment and depended on doing piece work on local farms from which he earned about Mk 10,000.00 (or £10) per month. Life was hard for him and his family.

In 2019, Harry was recruited for the carpentry training in Nkhotakota. After graduation Harry was given a carpentry tool kit and some start up raw materials and in 2020 Harry opened his own carpentry shop at a trading centre in his area. Business has been good for Harry and in a good month he earns up to Mk 80,000.00, increasing his income by 700%. This income has enabled Harry to provide more financial support to his mother, build a new three roomed house roofed with corrugated iron sheets, buy a bicycle and pay school fees for his young brother. In future Harry plans to build a bigger shop, buy electrical carpentry equipment and employ an assistant.

**Harry Ernest** ali ndi zaka 35 ndipo amakhala mboma la Nkhotakota, ku Malawi. Iye analumala mwendo. Bambo a Harry anamwalira iye ali wamng'ono motero Harry analeredwa ndi mayi ake amene amalima pongofuna kupeza chakudya (small holder farmer). Iwo analephera kupeza ndalama zolipilira sukulu mwana wao choncho Harry analekera sukulu ali folomu yachiwiri. Kamba kopanda mapepala a sukulu Harry analephera kupeza ntchito motero ankadalira kugwira maganyu mminda yoyandikana ndi kwao. Akagwira maganyu iye ankapeza Mk 10,000.00 pamwezi. Harry ndi mayi ake amakhala moyo osowa.

Mchaka cha 2019 Harry anatengedwa ndi a MACOHA kuti akachite nawo maphunziro a ukalipentala ku Nkhotakota. Atamaliza maphunziro ake Harry anapatsidwa zida ndi zipangizo za ukalipentala ndipo mu chaka cha 2020 Harry anatsekula malo opangira bizinezi ya ukalipentala pa malo a malonda a pafupi ndi kwao. Bizinezi yake yakhala ikumuyendera bwino Harry mwakuti malonda akayenda bwino amapeza ndalama zokwanira Mk 80,000.00 pa mwezi, kuchulukitsa ndalama zimene ankapeza poyamba ndi zikwi makumi asanu ndi awiri (700%).

Ndalama zimene Harry akupeza zamuthandiza kusamalira bwino mayi ake, kumanga nyumba ya tsopano ya njerwa, yofolera ndi malata, kugula njinga yopalasa komanso kulipilira sukulu mng'ono wake.

Mtsogolomo Harry ali ndi maganizo odzamanga malo akulu ogwilirapo ntchito yake, kudzagula zida za magetsi ndi kudzalemba munthu omuthandiza ntchito.



## BEN PAYNE

**Ben** has lived at Milltown Community in Aberdeenshire since 2015, where he volunteers in the tool refurbishment workshop. Whilst the volunteers work, they keep themselves happy, listening to the radio, chatting and having a laugh together. Ben enjoys refurbishing the smaller tools that are sent to Malawi, such as hatchets and hammers. He is always interested to hear about how the trainees and graduates are getting on and the project is developing. Outside of work Ben has a keen interest in politics, enjoys going to church and is a big supporter of Montrose Football Club.

**"I hope my work helps people like myself with a disability in Malawi to have a better income and quality of life."**

**Ben** wakhala ku Milltown Community mdela la Aberdeenshire kuyambila mchaka cha 2015, kumene amagwira ntchito yodziperuka pa malo okonzanso zida zowonongeka. Akamagwira ntchito anthu odziperekawa amadzisangalatsa pomvera wailesi, kucheza ndi kuseka limodzi. Ben amamva bwino akamakonzanso zida zing'onozing'ono zoti zitumizidwe ku Malawi, monga ngati nkhwangwa ndi nyundo. Nthawi zonse amakhala ndi chidwi kumva mmene ophunzira ndi amene anatsiriza maphunziro a kupangira komanso mmene ntchito yonse yophunzitsa ntchito za manja ikupitira mtsogolo. Kupatula kugwira ntchito Ben ali ndi chidwi ndi zandale, amakondanso kupita ku tchalitchi ndipo ndi otsatira wamkulu wa timu ya mpira ya Montrose.

**"Ndikukhulupilira kuti ntchito yanga ikuthandiza anthu ngati ine a ulumali ku Malawi kuti adzipeza ndalama zokwanira ndi moyo wabwino."**



# LUCY MTHALI



Lucy Mthali is 27 years old comes from Nkhatabay district, Malawi. She was born with a disability. Lucy went to school up to form two but left due to pregnancy. After delivery of her child Lucy could not continue with her education as there was no money for her school fees. She was worried about her future and how she would be able to support her child. However in April 2019 Lucy was selected to take part in the tailoring training programme. The course included lessons in basic business management, HIV and AIDS, organic manure production, gender awareness and reproductive health. After training Lucy received a sewing machine and some start up materials. When she came back home, Lucy rented a shop and started her tailoring business. She has been able to win the trust of many customers in her area and her monthly income has been in the range of Mk 20,000.00 to Mk 30,000.00 per month. Lucy no longer worries about her future and is able to support herself, her child and her family. Lucy is also able to pay for her child's pre-school education. Her future plan is to buy another sewing machine and employ an assistant to help her meet the demands of her customers. Lucy is very thankful to GCT Tools and Training for Livelihood Project for transforming her life and giving her hope for the futu

Lucy Mthali ali ndi zaka 27 amakhala mboma la Nkhatabay, mdziko la Malawi. Iye anabadwa ndi ulumali. Lucy analeka sukulu pa kalasi la chiwiri la maphunziro a ku sekondale chifukwa anali oyembekezera. Atachira Lucy analephera kupitiriza maphunziro ake chifukwa chosowa ndalama zolipilira sukulu. Iye anali ndi nkhwana ndi tsogolo lake komanso kuti adzasamala bwanjji mwana wake. Koma mchaka cha 2019 Lucy anasankhidwa kuti akachite maphunziro a utelala. Kumaphunziroko anaphunziranso za kayendetsedwe ka bizinezi, HIV ndi AIDS, kapangidwe ka manyowa, za kusasalana pakati pa abambo ndi amayi, ndi za uchembere wabwino. Atamaliza maphunziro ake Lucy analandira makina osokera ndi zipangizo zina za utelala.

Atabwelera kumudzi Lucy anapanga lendi nyumba yopangira bizinezi ndipo anayamba ntchito ya utelala. Masokedwe ake akukondweretsa anthu ochuluka mdela lawo ndipo akupeza ndalama za pakati pa Mk 20,000.00 ndi Mk30,000.00 pa mwezi. Tsopano Lucy sadela nkhwana za tsogolo lake ndipo akutha kudzisamalira komanso kusamalira mayi ake pamodzi ndi mwana wake. Lucy akukwanitsa kulipilira mwana wake sukulu ya mmera mpoyamba. Lucy ali ndi malingaliro ofuna kugula makina ena ndi kulemba ntchito munthu wina omuthandiza kukwaniritsa zofuna za ogula ake. Iye akuthokoza kwambiri ntchito ya Global Concerns Trust yopereka zida ndi luso la ntchito za manja chifukwa yasintha moyo wake.





## FRANK BANDA

---

We were sad to hear of the recent death of **Frank Banda**. Frank worked as MACOHA CBR District Manager in Nkhotakota between 2011 and 2020, when he retired. Frank's passion, dedication and excellent management skills led the team to successfully offer training and support to many people with disabilities within Nkhotakota district. Frank will be fondly remembered and sadly missed.

Tinadandaula kumva za imfa ya Frank Banda posachedwapa. Frank anagwira ntchito pa udindo wa Oyendetsa Ntchito ya MACOHA Mboma la Nkhotakota kuchokera chaka cha 2011 mpaka chaka cha 2020 pamene anapuma ntchito. Kukonda ntchito, kudzipereka ndi kuyendetsa bwino ntchito kunathandizira ogwira ntchito kuti apereke maphunziro ndi upangili kwa anthu ochuluka a ulumali mboma la Nkhotakota. Frank adzakumbukilidwa mwa chikondi komanso kusowedwa modandaula.



# TOOL WORKSHOPS



**(left to right) Lesley Barker, Robert Mitchell, Warren Canham, Kevin Marshall, Stewart Keith, Dhaoud Hussain, Malcolm Lindsay, Jamie Lusk.**

The tools and sewing machines are refurbished by groups of adults with learning difficulties, mental health difficulties, people with dementia and retired people. The quality of the tools and Singer sewing machines that are donated make them worth shipping across the world, as they are durable and can be repaired. They are also recycled. Without the input of the workshops in Scotland and Northern Ireland, we would be forced to buy tools and machines in Malawi, which are cheaply made, break easily, and cannot be repaired.

This project promotes skill development in Scotland and Malawi, engaging volunteers in international development, including people with learning and mental health difficulties across the UK. There are many skills involved in refurbishing the tools and machines, and the work can be adapted to suit any technical ability. The volunteers enjoy the social nature of the tools groups, and find it really rewarding to be helping individuals so directly in Malawi. In addition, this project contributes to a reduction of waste in the UK in terms of the recycled tools and sewing machines.

# MALO OKONZERA ZIDA



**Win Hatton, Warren Canham, Elizabeth Halliday, Malcolm Lindsay and Joseph Gibney modelling shirts made by one of our Malawian graduates, Waisanga Chakutanda.**

Zida ndi makina osokera zimakonzedwanso ndi magulu a anthu a ulumali ovutika pophonzira, wa kubongo ndi anthu opuma pa ntchito.

Ubwino wa zida ndi makina a mtundu wa Singa zimene anthu amapereka ndiwakuti ndizofikila pa mulingo oti zizitumizidwa ku maiko a kutali chifukwa ndi zolimba komanso zingathe kukonzedwanso. Ndi katundu yemwe angatheke kumusulanso (recycled). Pakanapanda ntchito imene imachitika ku malo okonzanso zida ndi makina ku Scotland ndi ku Mpoto kwa dziko la Ireland, tikanaumilizidwa kumagula zida ndi makina ku Malawi, zimene zimakhala zosalimba, zimasweka msanga komanso sikutheka kuzikonzanso.

Ntchito yophunzitsa maluso a manja ndi kupereka zidayi imapititsa patsogolo luso la manja ku Scotland ndi ku Malawi, kuthandiza anthu

odzipereka kuti atenge nawo gawo pa chitukuko cha maiko osiyanasiyana, kuphatikizapo anthu a ulumali ovutika pa maphunziro ndi anthu a ulumali wa kubongo ku Mangalande (UK). Pali maluso ochuluka amene amagwiritsidwa ntchito pokonzanso zida ndi makina zimenezi, ndipo ntchitoyi ingasinthidwe kuti igwirizane ndi kuthekera kwa mtundu uliwonse.

Anthu odziperekawa amasangalala ndi mgwirizano umene umapezeka mmagulu a anthu okonzanso zida ndi makinawa, ndipo amaona kuti kuthandiza anthu ku Malawi mwa chindunji motere ndi chinthu chopindulitsa. Kuonjezera apa ntchitoyi ikuthandiza kuchepetsa katundu otayidwa ku Mangalande kudzera mu kukonzaso zida ndi makina.





Quality in Life

Garvald Edinburgh is a Scottish Charity offering creative opportunities and support for people with learning disabilities. They are inspired by the ideas of the educator and philosopher, Rudolf Steiner and have been operating in Edinburgh since 1969.



Warren Canham, Brian Baird, Melinda Andrews, John Newey, Tony Schofield, Dhaoud Hussain, Joe Gibney, Liz Halliday, Kevin Murray

Garvald Edinburgh ndi bungwe la chifundo la mdziko la Scotland limene limapereka mwayi opanga zinthu mwatsopano ndi chithandizo kwa anthu a ulumali pa maphunziro. Iwo amalimbikitsidwa ndi maganizo a mphunzitsi komonso oganiza mozama (educator and philosopher) otchedwa Rudolf Steiner ndipo bungweli lakhala likugwira ntchito ku Edinburgh kuyambira mchaka cha 1969.

# MILLTOWN COMMUNITY

Milltown Day Workshop, South Aberdeenshire, was set up in 1996 to provide practical work activities for local people with a range of disabilities. Restoring tools has been one of our most popular activities in our Day Workshop for nearly 20 years. The work is done by people who have some disabilities, but more importantly are enthusiastic and like to have a good laugh!



**Back: Scott Fisher, Richard Firth, Michelle Parkinson, Alan Jeffrey, Ben Payne.  
Front : Simon Desborough, Duncan Smith**

Milltown Day Workshop ya ku mmwera kwa Aberdeenshire, inakhazikitsidwa mchaka cha 1996 kuti idzipereka ntchito za manja kwa anthu a ulumali osiyanasiyana. Kukonzanso zida ndi imodzi mwa ntchito zathu zodziwika kwambiri ku Day Workshop kwa zaka pafupifupi 20. Ntchitoyi imagwiridwa ndi anthu a ulumali, koma chofunika kwambiri ndi chakuti ndi anthu amene ali ndi chidwi ndi okonda kuseka.





# THE ECOLOGY CENTRE, FIFE

The Ecology Centre is a charity that brings people and nature together. They offer environmental education, volunteering opportunities and also create and manage habitats for wildlife.



Jim Stevenson, Pat Convery, Robert Smith and Fred Varney

Ecology Centre ndi bungwe la chifundo limene limabweretsa anthu ndi chilengedwe pamodzi. Limapereka maphunziro a za chilengedwe, mwayi wa ntchito yodziipereka komanso kukonza ndi kusamalira malo a nyama zakuthengo.



## Tools For Solidarity



Andrei, Felix, Eem, Daria, Roisin, Hamish and Stephen

There had been a tools group operating in Belfast since 1984. Tools For Solidarity arose from this group in 1992 and has been running a volunteer managed workshop since then. We have a team of international and local volunteers some of whom are people with disabilities/learning difficulties.

Ku Belfast kwakhala kuli gulu la zida kuyambira mchaka cha 1984. Bungwe la Tools for Solidarity linayambitsidwa ndi gulu la zidazo mchaka cha 1992 ndipo lakhala likuyendetsa ntchito ya anthu odzipereka kuyambira nthawi imeneyo. Tili ndi anthu odzipereka a konkuno komanso ena akunja amene ena mwa iwo ndi a ulumali wa pa maphunziro (learning disabilities).



Al, Emanuel, Sam, Stephen, John, Chris (holding Benje) and Caroline

**The Downpatrick** workshop opened its doors to volunteers in January 2004 in a workshop cold enough to ensure the volunteers stuck around - they stuck to all those freezing metal tools. The Downpatrick workshop is open to all and particularly welcomes people with mental health issues. The workshop is open 4 days a week and there are currently about 30 volunteers who drop in each week. We are delighted to work together with all the tools groups in Scotland to support GCT.

**Malo a Downpatrick** anatsegulidwa kwa anthu odzipereka mmwezi wa January 2004 pa malo ogwilirapo ntchito ozizila kuti ogwira ntchito akhalebe limodzi - anapitiliza kugwira ntchito ngakhale zida zinali zozizira. Malo amenewa a Downpatrick ndi otseguka kwa wina aliyense ndipo kwenikweni anthu a ulumali wa kubongo ali olandiridwa. Malo ogwilira ntchitowa amakhala otsegula masiku anayi pa sabata ndipo pali anthu odzipereka 30 amene amafika pamalopa sabata iliyonse. Ndife a chimwemwe kugwira ntchito pamodzi ndi magulu onse okonzanso zida kuti tithandize bungwe la Global Concerns Trust (GCT).



## THE MOURNE GRANGE CAMPHILL COMMUNITY

The Mourne Grange Camphill Community in Killeel runs a small workshop focusing on cane furniture making and carpentry kits.

Pa Mourne Grange Camphill Community ku Killeel pali malo ang'ono amene amakonzanso zida zopangira mipando ya nsungwi ndi za ukalipentala.



Neil Randall, Geoff Claxton, Conor O Hare and James Ferguson



## BEANNACHAR CAMPHILL COMMUNITY

Camphill Beannachar offers residential care and day work placements for young adults with learning disabilities.

Besides a strong land-based work programme with a farm, walled garden and 27 acre estate, Beannachar runs a variety of craft workshops and is delighted to host, since the summer of 2015, a part-time "Tools For Self- Reliance" tools workshop. Although currently a part- time workshop, it is very popular with the students and strongly supported over the past 10 years by the Ellon Rotary Club. We will be looking to run it full time in the future.



Top left to right: Daniel Sim, Connor Mackay, Steven Macdonald, Barry Ironside  
Bottom, left to right: Tilmann Reinardy, Grant Powrie, Alasdair Young, Amos Joyce-Breton

Camphill Beannachar imapereka chisamalira chogonera komweko ndi ntchito yogwira masana kwa achinyamata amene ali ndi ulumali wa pa maphunziro. Pambali pokhala ndi ndondomeko yokhazikika ya zo malo ndi munda olimapo, munda wa mumpanda ndi malo olima mbewu zosiyanasiyana okwanira ma ekala 27 (27 acre estate), Beannachar ilinso ndi malo angapo a zokonzakonza ndipo ndi a chimwemwe kuti kuyambira mmwavu wa 2015, anayambitsa ntchito yokonza zida kwa nthawi yochepa (part time) ya Tools for Self Reliance. Ngakhale ili ntchito ya nthawi yochepa pakali pano ophunzira amayikonda ndipo yakhala ikuthandizidwa kwambiri kwa zaka khumi zapitazo ndi bungwe la Ellon Rotary Club. Tikuyembekezera kudzapangitsa ntchito imeneyi mosayimitsa (full time) mtsogolomo.





Emily Banda



# IMPACT

To date over 540 adults with disabilities in Malawi have undergone training and received start up tools. The impact upon graduate trainees has been truly immense, with 97% having succeeded in setting up new businesses. We have recorded an average increase in income for trainees of 356%, and an increase in trainees' families' income of 248%.

In real terms this translates to a substantial improvement of living standards for trainees and their families; being able to afford better food, basic household goods, livestock, medicine, labour, agricultural tools, seeds, land rental, labour and even better housing. Graduate trainees have shown that their businesses are expanding, with 93% achieving economic self sufficiency and many able to invest in secondary businesses for the family. As significant as the increase of income to graduates, is the increase in their confidence, independence, and ability to plan for the future.



**Kenneth Maulana**



# IMPACT

Kufika lero anthu akuluakulu a ulumali oposerera 540 anapanga maphunziro ndipo anapatsidwa zida zoyambira bizinezi zawo. Miyoyo ya iwo amene anamaliza maphunziro yasintha kwambiri, ndipo anthu 97 mwa 100 aliwonse anakwanitsa kuyambitsa mabizinezi a tsopano. Tapeza kuti ndalama zimene akupeza anthu amene akupanga mabizineza zakwela ndi 356 pa 100 iliyonse (356%), ndipo ndalama zimene maanja awo amapeza zakwela ndi 248 pa 100 iliyonse (248%).

Kukwela kwa ndalama zimene akupeza anthu amene analandira maphunzirowa kukusonyeza kuti miyoyo yao pamodzi ndi ya maanja awo yapita patsogolo kwambiri; akukwanitsa kupeza chakudya chabwino, katundu wa pakhomo, ziweto, mankhwala, kulipira a ntchito, zida za ulimi, mbewu, kulipilira malo ngakhale kumanga nyumba za bwino. Otsiriza maphunzirowo aonetsa kuti mabizinezi awo akukula mwakuti 93 mwa 100 aliwonse ndi odzidalira pa chuma ndipo ambiri mwa iwo ali ndi kuthekera koyambitsanso mabizinezi ena a pa banja pawo. China chofunika kwambiri ngati kukwela kwa ndalama zimene ophunzira akupeza ndi kukwela kwa kudzikhulupilira kwao, kuyima paokha ndiponso kutha kukonza ndondomeko za mtsogolo.

This project is funded by the Scottish Government as part of the Scotland Malawi Partnership Agreement.

We would like to thank them, together with our partners KODO, MACOHA, The Scottish Tools for Self Reliance Workshops, The Ecology Centre and Tools for Solidarity for making this project possible.



**The Scottish  
Government**  
Riaghaltas na h-Alba



Written by Emma Duncan, Translated by Bernard  
Madziatayika and designed & printed by  
[www.treehouseprint.co.uk](http://www.treehouseprint.co.uk)

**The Global Concerns Trust is a  
registered charity in Scotland:**  
SC025640  
[www.globalconcernstrust.com](http://www.globalconcernstrust.com)

Ntchito imeneyi ikuchitika ndi thandizo  
la ndalama lochokera ku boma la  
dziko la Scotland ngati mbali imodzi ya  
mgwirizano wa pakati pa mayiko a  
Scotland ndi Malawi.

Tikuthokoza boma la Scotland,  
mabungwe amene tikugwira nawo  
ntchitoyi a KODO ndi MACOHA, Malo  
okonzanso zida zowonongeka a  
Scottish Tools for Self Reliance, Malo a  
zachilengedwe a Ecology Centre  
ndiponso malo okonzanso zida  
zowonongeka a Tools for Solidarity  
popangitsa kuti ntchitoyi itheke.



**The Scottish  
Government**  
Riaghaltas na h-Alba



Written by Emma Duncan, Translated by Bernard  
Madziatayika and designed & printed by  
[www.treehouseprint.co.uk](http://www.treehouseprint.co.uk)

**Bungwe la Global Concerns Trust ndi  
bungwe la chifundo limene  
linalembetsedwa ku Scotland:**  
SC025640  
[www.globalconcernstrust.com](http://www.globalconcernstrust.com)